



## Kalata Yofotokoza za Msonkhano wa 16 wa Sinodi ya Aepiskopi kwa Mbumba ya Mulungu

Abale ndi Alongo,

Pamene tikufika ku mapeto a zokambirana zoyamba za msonkhano wa 16 wa Sinodi ya Aepiskopi, tikuthokoza Mulungu pamodzi ndi inu nonse chifukwa cha nthawi yopambana imene takhala nayo pa msonkhano umenewu. Kuyambira pa 30<sup>th</sup> September, nthumwi zonse zochokera ku maiko onse a dziko lapansi, za zilankhulo ndi chikhalidwe chosiyanasiyana, takhala tikusinkhasinkha kuti timvetse tanthauzo lokhala *Mpingo woyendera limodzi* pofuna kukwaniritsa ntchito yofalitsa Mthenga wa Ambuye.

Ngati Akhristu, amene tili ndi udindo, mphatso ndi ntchito zosiyanasiyana m'moyo wathu, takhala tikupemphera ndi kukambirana za chuma ndi umphawi wopezeka mu Mpingo wathu. Pakumvetsera Mau a Mulungu ndi zochitika m'moyo wa ena, mwachimwemwe, taphunzira kucheza ndi Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera amene watiwunikira kuti tithe kumvetsera ndi kusinkhasinkha. Tinalinso ndi mwai wotha kuzindikira kufunika kokambirana zochitika m'moyo wa Mpingo wathu (Latin Tradition) ndi wa Abale athu aku *'Eastern Catholic Churches'*. Chinali chinthu chamtengo wapatali kwa ife kukambirana ndi anzathu azikhulupiriro zina. Pa nthawi yonse ya msonkhanowu, timalimbikitsidwa pozindikira kuti munali nafe limodzi m'mapemphero anu pamene ifenso tinali nthumwi zanu zokunenerani nkhawa zanu, mafunso anu ndiponso zina zomwe inu mumayembekeza.

Msonkhano wathu umachitika pamene dziko lapansi likukumana ndi zowawa ndi zokhoma zambiri zodzetsa nkhawa yayikulu m'mitima mwathu makamaka chifukwa chakuti ena mwa ife tikuchokera m'maiko amene mukuchitika ziwawa ndi nkondo. Tidapempherera onse okhudzidwa ndi nkhanza zopitilira muyeso; sitinawayiwalanso onse amene akupsyinjidwa ndi mavuto ndi mikwingwirima ndi ziphuphu zowaumiriza kutenga njira zoopsya posamukira ku maiko ena. Posonyeza umodzi ndi Akhristu onse ndiponso iwo amene akuthandiza kudzetsa chilungamo ndi Mtendere m'malo amene kuli zipwirikiti, tidawapempherera.

Mopephedwa ndi Apapa tidakhala chete ndi kusinkhasinkha pofuna kumvetserana mowunikiridwa ndi Mzimu Woyera. Pamene timachita mapephero ochezera, limodzi ndi anzathu azipembezo zina, tinazindikira momwe aliyense amafunitsitsira kukhala mu umodzi monga tinachitiramu; ndipo izi zinatipangitsa kumvetsetsa za chiphunzitso cha a Ambuye Yesu cha kuti tikhale amodzi monga Iye ndi Atate ali amodzi. (Yohane 17:21). Mtanda ndi chida chophunzitsira chimene Ambuye adachigwiritsa ntchito, pamene Iye adakhala mmphawi chifukwa cha ife kuti ndi uphwawi wakewo ife tikhale olemera (2Akorinto 8:9).

Molumikizana kwathunthu m'chiyembekezo chimene chidadza kupyolera M'kuuka kwake, tidakhala ndi mpata wokambirana ndi abale ndi alongo molemekezana ngati anthu amene tidalandira ubatizo umodzi. Tidaphunziranso kumvetsera kulira kwa dziko lapansi ndi kwa anthu. Pogawana mozama zochitika m'moyo wathu, tinathandizika kuzindikira zimene Mzimu Woyera akufuna



kulankhula kudzera mu Mpingo wake masiku ano. Monga pa chitsime paja, pamene Yesu adakumana ndi mai wachisamariya kapena panjira yopita ku Yeriko, Chikondi chimalakalaka kuti, ovutika amene ndi abale ndi alongo athu, nawonso akoneddwe. Kukhala pafupi, kukoma mtima ndi chifundo: zimenezi ndiye chitsimikizo cha Kudziwulula kwa Mulungu Atate. Ichinso, chikuyenera kukhala chizindikiro chodziwika cha Ophunzira a Ambuye Yesu amene adayitanidwa kuti agwirizane ndi Mzimu Woyera popereka ulemu kwa Mulungu Atate ndi potenga nawo mbali pa chipulumutso cha dziko lonse lapansi.

M'mene masiku amatha, tidamvetsa koposa kuti, Mpingo ukuyitanidwa kuti utumikire mwachikondi chonga chimene Mulungu adakonda nacho dziko lapansi (Yohane 3:16). Pamene anthu osowa pokhala amene adasonkhana ku bwalo la Petro Woyera, adafunsidwa zomwe ankayembekezera kuti msonkhano wa Sinodi ukwaniritse; iwo adayankha kuti: “Chikondi”. Pamene zokambirana zapakatikati pa msonkhano zidasindikizidwa pa 15 October, tsiku limene lidali chaka chokumbukira Tereza Woyera wa Yesu, Papa Francisko adatsindika kuti, chikondi chimenechi chikuyenera kukhala thime lake la Mpingo, chikondi chowoneka mu Utatu Woyera ndi m'Sakramenti la Ukaristia chimene tingathe kukhala nacho pokhulupirira ndi pakudzikhuthula kwathunthu kwa Mulungu. Monga Apapa akunenera, izi zimasowa kulimba mtima kwakukulu ndiponso ufulu waukulu wofumira mumtima. Izi ndi zimensenso tidayesera kukwaniritsa pazokambirana zathu pokhala omasuka kufotokoza zimene tinkagwirizana komanso mfundo zimene tinkasiyana maganizo kuphatikizapo zolakalaka ndi mafunso athu.

Nanga tichitenji tsopano? M'miyezi yotsatirayi, yomwe ndi chigawo chachiwiri cha zokambirana zomwe zidzachitike m'mwezi wa October 2024, tikufuna kuti aliyense adzatenge nawo mbali kwathunthu pa mgwirizano wa utumiki wamphamvu monga liu loti Sinodi limatanthauza. Izi sinkhambakamwa chabe, ai, koma zochitika zenizeni zokhazikika m'moyo wa Mpingo kuchokera kwa Apostoli. Monga Apapa adatsindika kumayambiriro a Sinodi, chiyanjano ndi utumiki zitha kukhala ngati zinthu zam'malere pokhapokhapo ngati tiziwonetsera poyera ndi *kuzichita mooneka chamaso ngati Mpingo woyendera limodzi...(...)* polimbikitsa aliyense kuti azitenga nawo mbali (October 9, 2021). Pali zovuta ndi mafunso ambiri: Lipoti la zotsatira za msonkhano woyamba, zidzasonyeza mfundo zimene msonkhano udagwirizana komanso mafunso amene adafunsidwa ndi kufotokoza m'mene tingapitirizire kugwira ntchito pamodzi. Mpingo umasowa aliyense pofuna kupita patsogolo m'kusinkhasinkha kwake. Kwenikweni umasowa upangiri wa Ansembe ngati athandizi a Episkopi: utumiki wao wopereka masakramenti ngosowekera kwambiri pa moyo wa Mpingo wa Ambuye. Ukuyenera kudziwa kufunikira kwa udindo wa madikoni amene amatumikira makamaka anthu ofooka pakati pathu.

Mpingo ukuyeneranso kumvetsera Akhristu eniake, akazi ndi amuna --- umboni wa akatekisti amene, nthawi zambiri amakhala oyambirira kulalika Mthenga wa Ambuye. Ukusowekanso kumvetsera ndi chidwi zolakalaka za achinyamata, maloto ndi nzeru za anthu achikulire. Ukuyenera kutsitsimutsidwa ndi liu la uneneri la anthu odzipereka m'zipani za mu Mpingo ndi alonda amene sagona polalika Mthenga Wabwino. Ukuyenera kumvetsera mabanja, nkhwana zao pa za maphunziro komanso pa umboni wachikhristu umene amawuonetsa pa dziko lapansi masiku ano. Ukuyenera kulandira mau ndi maganizo a onse ofuna kutenga nawo mbali posinkhasinkha ndi kupanga ziganizo zoyendetsera Mpingo. Ukuyenera kumvetsera mwachifundo kulira kwa iwo amene adazunzidwa ndi zochitika zoipa za Akhristu. Ukuyenera kumveranso onse amene sakhulupirira nawo chikhupiriro cha Chikatolika koma amayesetsa kufunafuna choona ndipo



amene Mzimu Woyera amakhalanso mwa iwo (*Gaudium et Spes* 22, 5).

M'dziko limene timakhalali, momwe timapemphedwa kukonda ndi kutumikira, ngakhale pakati pa maphunzitso otsutsana, Mpingo ukuyenera kulimbikitsa mgwirizano m'madera onse a utumiki wake. Iyi ndiye njira yeniyeni yoyendera limodzi ngati Mpingo womwe Mulungu akuyembekeza m'zaka zamakono ano (Papa Francisko, October, 17, 2015). Sitiwopa konse kukwaniritsa pempholi. Maria, Amai a Mpingo, amene ndi woyamba pa ulendowu, amatsagana nafe pa ulendo wathu. Pachisangalalo kapena pamavuto, amatisonyeza Mwana wake amene amakhala nafe. Ndipo Yesuyo, ndi chiyembekezo chathu!

*Vatican City, October 23, 2023*

世界代表司教会議（シノドス）第16回通常総会『神の民への手紙』  
⇒<https://www.cbcj.catholic.jp/2023/10/27/28118/>



Kalata Yofotokoza za Msonkhano wa 16 wa Sinodi ya Aeposkopi kwa Mbumba ya Mulungu  
⇒<https://www.synod.va/en/news/letter-of-the-xvi-ordinary-general-assembly-of-the-synod-of-bishops-to-the-people-of-god.html>

